# LIU LA NAMIKANGO

Namikango Mission

**Volume 18(1), March 2018**


## Kuyamba Kwa Ziphunzitso za Mzigawo za Mu Luka 15

Chikhumbokhumbo cha zigawo zimenezi chidachokera ku nthambi yoona za Baibulo pa Mishoni ya Namikango chaka chatha: Luka 15. Kumayambiriro kwa Luka 15, tikuona Yesu akudya ndi okhometsa misonkho komanso anthu ochimwa, ndipo Afarisi komanso aphunzitsi a Chilamulo ali pomwepo, kung'ung'udza pa zimene Yesu akuchita. Chifukwa cha kung'ung'udza kwa anthu amadziyesa olungamawa, Luka akuti Yesu anawauza fanizo. Fanizo limodzi, nkhani zitatu, cholinga chakuti tidziwe kuti nkhani zimenezi zikuyenera kuyendera limodzi.

Chaka chino, Liu liyang'ana nkhani zitatu zimenezi. Liu la ulendo uno likamba za nkhani ya M'busa Wabwino ndi nkhosa yotaika; lotsatira idzakamba za nkhani ya mzimayi wabwino ndi ndalama yotaika; ndipo yachitatu idzakhala ya Atate Wabwino ndi ana ake awiri otaika. Kenako kudzakhala Liu lachinayi imene idzabweretsa nkhani zonsenzi pamodzi ndi kuzigwiritsa ntchito ku miyoyo yathu masiku athu ano.

Ngati sindinu m'Kristu, ndipo simunawerengepo Baibulo, koma mukufuna mutaphunzira pa zam'mene Mulungu amakuonerani komanso m'mene Yesu alili, apa ndi pabwino kuyambira. Koma ngati mwakhala muli m'Kristu kwa zaka zambiri, kulibenso malo ena oti muzame oposa ano. Ine ndikupezeka mu gulu lachiwiri, m'Kristu. Ndipo pamene ndikukhala ndi nthawi yolingalira fanizo limeneli, ndi zophweka kuona chifukwa chake limatchedwa uthenga wabwino mkati mwa uthenga wabwino.

Monga wina adanena, fanizoli limapanga dziko lokhalamo, ngati nyumba yaikulu, ya zipinda zambiri, ndi mazenera owonera kunja koma oyang'ana kosiyana. Pamene ukukhala m'nyumba imeneyi nthawi yaitali, ndi pamene umayamba kuona dziko mosiyana. Mu fanizo limeneli, Yesu akutifotokozera za mitu yambiri yaikuluikulu ya m'Baibulo; tchimo, kulapa, chikhululukiro, ndi zina zambiri. Fanizoli likukamba za njira zambiri zosiyana siyana zam'mene tingataikire, kulekanitsidwa ndi Mulungu. Likukamba za mtundu onse wa anthu kuyambira pa nthawi ya kulengedwa mpaka kuchimwa.

Koma fanizoli limakamba kwambiri za ine ndi inu, pa zam'mene tilili otaikira. Nkhani yomaliza mu nkhani imeneyi imakonda kutchedwa kuti fanizo la "mwana wolowerera." Liwu lakuti wolowerera likhoza kutanthauza, "kugwiritsa ntchito mpaka zonse Zitatha." Tikawerenga nkhaniyi, tikuona kuti zimenezi zikukambanso za atate, mzimayi, m'busa; ili ndi lokhudza Yesu, amene amapereka chikondi chonse chimene ali nacho ndi cholinga chakuti apeze ndi kubwezeretsa chotaikacho.

Pamene mukuwerenga, tikukulimbikitsani kuti mukhale ndi nthawi; lingalirani ndi kupemphera pamene mukuwerenga. Ganizirani muli mu nkhaniyi. Ganizani za anthu amene ali mu nkhaniyi komanso kuti inuyo mungadziyerekeze ndi ndani. Ndi pemphero lathu kuti pamene mukuwerenga, mudalitsike ndi mphatso ya mtengo wapatali ya fanizo limene watipatsali. Muone chinachake chokhudza Mulungu chimene simunachionepo m'mbuyomu. Madalitso a Mulungu akhale pa inu nonse.

-Ben Hayes

Pofuna kuti awerengi athu amvetse bwino phunziroli, tatenga mau ambiri mu Chichewa cha lero chopezeka mu Buku loyera *(Copyright 1988 by The Bible Society of Malawi).*

# Fanizo la Nkhosa Yosokera



Mu buku la Luka 15, Yesu akufotokoza mafanizo atatu pakuyankha zodandaula za Afarisi. Tikawerenga mu Luka 15:1-2 timamva kuti Afarisi anakwiya kwambiri ndi Yesu chifukwa analandira ndi kudya ndi anthu ochimwa komanso okhometsa misonkho. Afarisi adali anthu amene amatsata Chilamulo mosamala kwambiri, ndipo amatsata malamulo okhudza chiyero kuti munthu akhalebe oyeretsedwa monga mwa mwambo. Iwo amakhulupilira kuti Mulungu amasangalatsidwa ndi anthu okhawo amene amakhala odziyeretsa malingana ndi miyambo, ndi kuti amakonda anthu okhawo amene amatha kutsata Chilamulo mosamalitsa kwambiri.

Aliyense amene anali ochimwa, anali odetsedwa, ndiye Afarisi amayesetsa kuti akhale kutali kwambiri ndi anthu oterewa. Ichi ndi chifukwa chake anakwiya kwambiri ndi Yesu pakulandira ndi kudya ndi anthu ochimwa. Yesu amacheza ndi anthu odetsedwa, otaika, ndipo pakudya nawo Yesu amadziika pa chiopsezo chachikulu chokhala odetsedwa! Kodi ndi mphunzitsi wanji amene angalandire ochimwa komanso kumadya nawo?

Chifukwa cha kung'ung'udza kumeneku, Yesu akufotokoza za mafanizo atatu ku gulu limene lasonkhana, m'mene munali Afarisi ndi anthu aja amatchedwa ochimwa. Timawerenga fanizo loyamba mu Luka 15:3-7. Iyi ndi nkhani yodziwika bwino, ya nkhosa Yosokera komanso m'busa wabwino. Mu nkhani imeneyi, m'busa akuzindikira kuti nkhosa imodzi palibe. Poyamba anali ndi nkhosa 100, koma pano ali ndi 99 zokha. Nthawi yomweyo m'busa akusiya nkhosa 99 zija ndi kupita kukayang'ana nkhosa yotaika ija.

Tikuona kuti iye akupita ku nkhalango kuti akathe kuyang'ana bwino bwino. Iye akuyang'ana ku chigwa ndi m'mapiri mpaka ataipeza nkhosa yotaikayi. Ndipo pamene m'busayu wapeza nkhosa yakeyi, waiika pa phewa pake ndi kuitengera kumene kuli nkhosa zinzake, ku malo ake. Pamene nkhosayi yabwerera kumene kuli zinzake, iye akusangalala ndi anzake, ndipo ali odzadzidwa ndi

## Luka 15:1-7

**Koma amisonkho onse ndi anthu ochimwa analikumyandikira kudzamva Iye. Ndipo Afarisi ndi alembi anadandaula nati, Uyu alandira anthu ochimwa nadya nao. Koma anati kwa iwo fanizo ili, nanena, Munthu ndani wa inu ali nazo nkhosa makumikhumi, ndipo pakutayika imodizi ya izo, sasiya nanga m'chipululu zinazo makumi asanu ndi anai mphambu zisanu ndi zinai, nalondola yotayikayo kufikira aipesa? Ndipo pamene adaipenza, aisenza pa mapewa ake wokondwera. Ndipo pakufika kunyumba kwake amema abwenzi ake ndi anansi ake, nanena nao, Kondwerani ndi ine, chifukwa ndinapeza nkhosa yanga yotayikayo. Ndinena kwa inu, kotero kudzakhala chimwemwe Kumwamba chifukwa cha wochimwa mmodzi wotembenuka mtima, koposa anthu olungama makumi asanu ndi anai mphambu asanu ndi anai, amene alibe kusowa kutembenuka mtima.**

chimwemwe chachikulu chifukwa wapeza nkhosa yake imene inataika ija.

M'busa wabwinoyu sakuisiya nkhosayi kuti ikhalebe yotaika, kapenanso kusiya kuiyang'ana pamene akuvutika kuipeza mu nkhalango. M'busa wabwino saisiya nkhosa yotaikayi, koma m'malo mwake akufunitsitsa ataipeza nkhosa yakeyi ndi kuibweretsa kumalo abwino. Mu nkhalango ndi malo oopsa kwambiri kuti nkhosa itaike. Pamene nkhosa yachoka mu gulu la zinzake komanso ku chitetezo cha m'busa, imapezeka kuti yazungulilidwa ndi imfa.

Mu nkhalango mumakhala nyama zolusa zimene zingakonde kuti zidye nkhosa. Komanso, popanda kutsogoleredwa ndi m'busa, nkhosa ikhoza kugwera kuphompho, kuthyola mwendo, kukhala ndi njala komanso kufa kumene. Tikudziwanso kuti nkhosa yosokera imavutika

kuti ipeze njira yoti ibwerererere kunyumba. Nkhosa siingathe kuzindikira njira imene inadzera ngakhale kufunsa zam'mene ingayendere. Choncho, pamene nkhosa yataika, imakhala yotaika, ndipo imakhala mu nyengo yoopsa.

Ngakhale kuti nkhalango ndi malo oopsa odzadza ndi nyama zamtchire zoopsa komanso malo ake ovuta, m'busa salola kuti zimenezi zimukanikitse kufuna nkhosayi. Iye amafunafunabe, kwinaku akulimbana ndi nyama zoposa ndi kuyang'ana mu phompho, m'phanga, m'chigwa komanso m'mapiri. Kodi Yesu akuti m'busa wabwino ameneyu akuchita chiyani pamene wapeza nkhosa yotaikayi? Kodi m'busayu akumenya nkhosayi chifukwa chothawa? Kodi m'busayu akuipondaponda ndi kumaitchula maina? Kodi m'busayu akuiwuza kuti yachimwa ndiye chifukwa cha chimenechi ikuyenera kuti ikhale mu nkhalango muja moyo wake onse?

Ayi! Pamene m'busa wabwinoyu wapeza nkhosa yotaikayi, iye akuiika pa phewa pake mosamala ndi kuitengera kumene kuli zinzake. Mu njira yomweyo, pamene Mulungu wapeza munthu otaika, atamusakasaka kenako mkumupeza mu nkhalango, Iye samumenya kapena kumutchula maina kapena kunena kuti afere m'chipululu. M'malo mwake, monga Iye m'busa wabwino, Mulungu amanyamula munthuyu kumupititsa kukhola la nkhosa, ndi kumubwezeretsa kwa iye mwini. M'busa wabwino akudziwa kuti sizokwanira kungopeza nkhosayi m'nkhalango. Iye akuyenera kupereka mphamvu komanso chitetezo chake ndi cholinga chakuti ayitulutse nkhosayi m'nkhalango ndi kuitengera kumalo abwino. M'busa wabwinoyu sakusamala za chitetezo chake ndipo akupita m'nkhalango kuyang'ana, ndi kugwiritsa ntchito mphamvu zake zonse kunyamula nkhosayi kupita nayo kunyumba.

Yesu akunena kuti nkhosa Yosokerayi ikabwerera ku gulu la zinzake, m'busayu amakhala osangalala chifukwa cha kubwereraku ndipo amaitana anzake kuti adzasangalale naye pamodzi. M'busayu amakonza phwando losangalalira kupezeka kwa nkhosayi, ndipo Yesu akuti mu njira yomweyo kumakhala chisangalalo kumwamba pamene ochimwa m'modzi watembenuka mtima.

Nkhani ya fanizo la M'busa Wabwino ndi la mtengo wapatali m'Chipangano Chatsopano. Mu fanizo limeneli la M'busa Wabwino, komanso fanizo lotsatira la Mzimayi wabwino (Fanizo la ndalama yotayika) (Luka 15:8-10), lemba likuti Mulungu amakhala ndi chisangalalo chachikulu pamene ochimwa walapa, kapena pamene wotayika wapezeka ndi kubwezeretsedwa. Awa ndi malo okhawo m'Chipangano Chatsopano amene tikupeza liwu lakuti "chisangalalo" kunena za Mulungu mwini. M'mau ena, m'Chipangano Chatsopano chonse, ndi mu buku la Luka 15 lokha limene tikuona kuti Mulungu akupeza chisangalalo mu chochitika chinachake, ndipo chisangalalo chimenechi chili mu kupeza anthu otayika ndi kuwabwezera kwa Iye mwini. Mulungu samangopeza chisangalalo kokha pakupeza anthu otayika, koma ichi ndi chimene chimamubweretsera chisangalalo chonse! Uwutu si uthenga wabwino kokha kwa ife, iyi ndi nkhani yabwino! Mulungu wathu, M'busa Wabwino, amakonda kupeza nkhosa zotayika.

Mu fanizo limeneli la nkhosa yosokerayi, tikuona chikhumbokhumbo cha Mulungu chikukhala m'kupezeka kwa nkhosa komanso kuibwezeretsa. Mulungu sizimamukhudza kuti nkhosayi yasokera mu nkhalango kumene kuli nyama zoopsa. Iye akupita kukafuna nkhosa zotaikazi, ndipo iye sasiya mpaka atazipeza ndi kuzibweretsa kunyumba. Yesu akupitirira ndi fanizo limeneli patsogolo, pakulengeza kuti iye ndiye m'busa wabwino. Mu Yohane 10:11-18 Yesu akuti mu njira yomweyi m'busa akutaya moyo wake kuti apulumutse nkhosa, choncho Yesu anataya moyo wake ndi cholinga chakuti abweretse otaika kwa Mulungu. Monga m'busa wabwino ali ndi cholinga choyambirira, ndipo chimenechi ndicho kupeza nkhosa yotaika.

Monga m'busa wabwino mu Luka 15, Yesu akutiuza kuti amadziwa nkhosa zake ndipo nkhosa zakezo zimamva mau ake. Iye akamaziitana nkhosa zakezo, zimadziwa kuti ndi m'busa wawo wabwino amene akuitana ndipo zimamutsatira. Mu Yohane 10, Yesu akutikumbutsa kuti m'busa wabwino amaona kuti moyo wa nkhosa ndi ofunikira kuposa wake.

M’malo mwake, m’busa wabwino amataya moyo wake chifukwa cha nkhosa. M’busa wabwino amapita ku nkhalango yoopsa, kuika moyo ndi chitetezo chake pa chiopsezo, zonsenzi chifukwa cha nkhosa. Ichi ndiye chinthu choyambirira chimene m’busa wabwino chimamukhudza, ndipo chimenechi ndi chimene Yesu chimamukhudza. Yesu akuti m’busa amachita zinthu zonsezi, “ndi cholinga padzakhale gulu la nkhosa limodzi ndi m’busa m’modzi” (Yohane 10:16).

Yesu ndi m’busa wathu wabwino, ndipo chokhumba chake ndi chakuti tonse tibwere ku nkhosa za Mulungu. Yesu akufunitsitsa kuti nkhosa zake zikhale pamodzi, kukhala mwa umodzi ndi mtendere. Nkhosa ikasowa kapena kusokera m’nkhalango, Yesu sayisiya nkhosayi kuti ikhale m’menemo. M’malo mwake, iye amapita kukaisaka mpaka ataipeza, ndipo amagwiritsa ntchito mphamvu zake kuibweretsa nkhosayi ku khola. Iyi ndi nkhani yabwino kwa nkhosa, kaya tipezeka mu khola la Mulungu, kapena kutaika m’nkhalango. Tili ndi m’busa wabwino, Yesu, amene amakonda kupeza nkhosa, ndipo amakonda kusangalala pamene zipezeka ndi kubwezeretsedwa. Amen!

Pezani nthawi kulingalira fanizo la nkhosa yosokera mu Luka 15:3-7. Gwiritsani ntchito mafunso awa kuti akutsogolereni:

1. Mukawerenga Luka 15:3-7, kodi mukuphunzira chiyani chokhudza Mulungu?
2. Kodi m’busayu akuchita nayo chiyani nkhosa yotaika ija ikapezeka?
3. Mukawerenga ndime imeneyi, mukuphunzira chiyani chokhudza anthu?
4. Werengani Yesaya 53:6. Yesaya akuti tili ngati nkhosa zimene zasokera. Kodi ndi mu njira ziti zimene mungathe kuchita ngati nkhosa zosokera?
5. Malingana ndi Yesaya 53:6 ndi Luka 15:3-7, pamene mwachita ngati nkhosa yosokera Mulungu amachita chiyani kwa inu?
6. Kodi mu uthenga wabwino uliwonse mu Luka 15:3-7? Ngati ndi choncho, ndi wakuti chiyani?
7. Tsopano mwamvetsetsa fanizo la nkhosa yosokera mu Luka 15 komanso kuti Mulungu ndi m’busa wanu wabwino, kodi inu mwayenera kuchita chiyani kwa Mulungu?
8. Ngati fanizo la nkhosa yosokera ndi nkhani yabwino kwa inu, mungagawe bwanji uthenga wabwinowu kwa anzanu?

-Eric Gephart

## Zowerenga Zina

Mutatha kuwerenga Luka 15:3-7, kodi mukufuna mutazama? Chithunzithunzi cha m’busa wabwino chikupezeka m’malo ambiri m’Baibulo. Chimenechi ndi chithunzithunzi chimene Mulungu akugwiritsa ntchito pakufotokoza zam’mene amasamalira ndi kuyang’anira anthu. Tikuona Yesu akufotokoza za anthu amene amawatumikira kuti ndi nkhosa zimene zili zotaika. Chithunzithunzi chimenechi cha Mulungu monga m’busa wabwino amene amasamalira anthu ake (nkhosa), chikutionetsa mtima wa Mulungu. Iye sakufuna kuti wina aliyense akhale otayikabe, koma iye akupita kukayang’ana anthu, ngakhale m’nkhalango, ndi cholinga chakuti awabweretse mu khola lake monga nkhosa. Pezani nthawi yoti muwerenge ndi kulingalira Baibulo pa ndime zotsatirazi:

Masalimo 23:1-6
Yeremiya 23:1-8
Ezekieli 34:11-16
Marko 6:30-44
Yohane 10:1-18

Pamene mukuwerenga ndi kulingalira pa ndime zimenezi, yankhani mafunso atatu awa:

1. Kodi mutu ndi ndime zimenezi zikundiuza chiyani za Mulungu?
2. Kodi mutu ndi ndime zimenezi zikundiuza chiyani za anthu?
3. Kodi ndiyenera kuchita chiyani pakusonyeza kumvera mutu ndi ndime zimenezi?